



UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

NYENGO MSABATAYI

KUYAMBIRA PA 12 MPAKA 18 AUGUST, 2024

NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI


Kuyambira Lolemba pa 12 August mpaka Lachitatu pa 14 August nyengo yadzuwa, yotentha, yafumbi ndi changululu ipitilira m'madera ambiri. Usiku ndi m'bandakucha kuzikhala kwa nyengo yozizira mmadera ena. Kenako kuyambira Lachinayi pa 15 August tiyembekezere nyengo yamphepo ndi mitambo yochuluka ndi kuthekera kwa mvula yowaza ndi yamawawa mmadera ena kuyambira m'madera akum'mwera kufalikira pakati ndi kumpoto. Panyanja zathu monga ya Malawi ndi Chilwa padzakhala mafunde okula chifukwa cha mphepo ya Mwera m'nthawi. Izi zizakhala chonchi kamba ka mphepo zozizira komanso zachinyontho kuchokera m'nyanja yamchere ya India kufikira ku Malawi.

Yellow to red – Kutentha koposa nyengo yokhazikika
Blue – Kuzizira koposa nyengo yokhazikika


NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

Nyengo yofunda kuposera mlingo wanthawi yayitali kunapitilira m'sabatayi makamaka masana pofananiza (Onani mapu kumanja) ndi usiku womwe m'madera ambiri kumazizilirapo kuposera mlingo wakazizilidwe wanthawi yayitali mbuyomu yamwezi wa August (Onani mapu pansipa). Chithuzithuzi chikuonetsa kuti kunazizira kwambiri ndi ku Mzuzu Airport ndi **6.7°Celcius** pa 8 August, 2024 pamene komwe kunatentha mowonjeza ndi kwa Ngabu ndi **36.2°Celcius** pa 11 August, 2024.

Minimum Temperature Anomalies (5-11 August 2024)



Maximum Temperature Anomalies (5-11 August 2024)



Potengera mlingo wa nthawi yayitali ku Dedza ndi komwe kunafunda kwambiri kuposera mlingo wake ndi madigiri **+7.3°Celcius** pa 6 August ndipo masana kunatentha ndi madigiri **29.0°Celcius**. Ku Mimosa m'boma la Mulanje ndi komwe kunazizira kwambiri pofananiza ndi mlingo wake wakuzizira wanthawi yayitali ndipo madigiri anafika **7.7°Celcius** pa 10th August 2024 womwe mlingo wozizira ndi madigiri **-8.3°Celsius** kusiyanana ndi mlingo wanthawi yayitali.

MALANGIZO M'SABATALI

- Tikhale osamala panyanja nthawi yomwe kuli mphepo ya Mwera.
- Tivale zovala zozitetezera ku nyengo yozizira kukamazizira makamaka ana and okalamba, komanso odwala mphumu (asthma).